Kodi aliyense amalandira kubadwa kwatsopano?

______________________________

==========================================================================

4. Ayi, sialiyense amene amalandira. Ndi okhawo amene amakhulupirira mwa Yesu. Ndi okhawo amene amalandira Iye. Mwina Nikodemo anayamba kumvetsetsa pamene anamva mawu amenewa.

Yohane 3:16:

> Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wokhulupirira Iye asatayike, koma akhale nawo moyo wosatha.

Kodi ndani anauza Nikodemo kuti yense wokhulupirira Iye akhale nawo moyo wosatha?

______________________________

==========================================================================

5. Yesu ndiye ananena zimenezi. Iye analankhula za iwo amene anakhulupirira mwa Iye. Koma kukhulupirira mwa Iye sikutanthauza kunena kuti, "ndikhulupirira." Kukhulupirira mwa Yesu kumatanthauza kulandira Mawu ake. Kumatanthauza kuvomereza kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu. Kumatanthauza kulandira zomwe Iye anadzera kudzachita. Kumatanthauza kumva chisoni chifukwa cha machimo amene anayambitsa kuti Yesu adze m'dziko lapansi kudzatifera. Ngati munthu wakhulupirira mwa Yesu ndiye kuti iye walandira kanthu kena.

Kodi ndi kubadwa kotani kumene okhulupirira mwa Yesu amalandira?

______________________________

==========================================================================

6. Iye amalandira kubadwa kwatsopano. Iye akhoza kulowa Ufumu wa Mulungu. Chimenechi ndi chimene Yesu anauza Nikodemo. Iye anamuuzanso kuti amene akhulupirira mwa Iye akhoza kukhala ndi moyo wina watsopano.

Yohane 3:14-15:

> Ndipo monga Mose anakweza njoka m'chipululu, chotero Mwana wa munthu ayenera kukwezedwa; kuti yense wakukhulupirira akhale

nawo moyo wosatha mwa Iye.

Kuchokera m'ndime zimenezi, kodi ndi moyo wotani umene wokhulupirira mwa Yesu amalandira?

______________________________

---

7. Iye amalandira moyo wosatha. Koma iye ayenera kukhulupirira mwa Mwana wa munthu. "Mwana wa munthu," linali dzina limene Yesu analigwiritsa ntchito podzitchula yekha. Limaonetsa kuti ngakhale kuti Iye anali Mulungu anakhala munthu. Anthu ayenera kuona Yesu. Yesu anakumbutsa Nikodemo pa zomwe zinaoneka kwa anthu aku Israeli. Iwo anali kulumidwa ndi njoka. Mulungu anauza Mose kuti apange njoka ndi zinthu zina zonga chitsulo. Iye adauzidwa kuti aike njokayo pamalo omwe anthu anakhoza kuiona. Pamene anthu anapenya pa njokayo anali kuchiritsidwa kumavuto awo olumidwa ndi njoka. Iwo anali kukhupirira kuti chimenechi ndicho chimene chikadakhoza kuŵathandiza.

Kodi ife tiyenera kuchita chiyani mwa Yesu m'malo mwakuti tilandire kubadwa kwatsopano ndi moyo wosatha?

______________________________

______________________________

---

8. Tiyenera kukhulupirira mwa Iye. Komatu siyense amene amakhulupirira ayi. Choncho siyense amene amalandira zomwe Yesu amafuna kuzipereka.

Kuchokera ku Mawu a Yesu akwa Nikodemo, kodi ndani amene amalandira kubadwa kwatsopano ndi moyo wosatha?

______________________________

______________________________

---

9. Ndiyense amene akhulupirira. Yense amene akhulupirira amalandira moyo wosatha. Taonani pa Mawu a Yesu.

Yohane 3:16:

Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa wana wake wobadwa yekha, kuti yense wokhulupirira Iye asatayike, koma akhale nawo moyo wosatha.

Anthu ena sakhulupirira mwa Yesu. Kuchokera m'ndime imeneyi, kodi ndani amene adzakhala ndi moyo wosatha? ______________________________

______________________________

==========================================================

10. Iwo sadzakhala ndi moyo wosatha. Iwo sadzakhala wobadwa mwatsopano. Yesu anauza Nikodemo kuti aliyense wokhulupirira mwa Iye adzakhala ndi moyo wosatha. Zimenezi zisananenedwe Yesu anali kulankhula za Ufumu wa Mulungu. Tsopano Iye ali kulankhula za moyo wosatha. Zinthu ziŵirizi zimayendera pamodzi. Ngati mutaloŵa Ufumu wa Mulungu muli ndi moyo wosatha mumaloŵa ufumu ndipo mumabadwa kwatsopano. Koma anthu ena sanabadwe kwatsopano ndipo alibe moyo watsopano. Yesu anati iwo adzaononegeka kapena adzafa.

Kodi ndi chifukwa chiyani chimene iwo adzafere? ______________________________

______________________________

==========================================================

11. Iwo adzafa chifukwa sakhulupirira mwa Yesu. Yesu anati mwana wa munthu ayenera kukwezedwa. Iye ananena kuti Iye ayenera kukwezedwa monga momwe Mose anakwezera njoka m'chipululu. Nikodemo anadziŵa zomwe Yesu anali kulankhula. Iye anadziŵa mmene njoka inalumira anthu. Anadziŵa mmene Mose anapangira njoka ndi kuipachika pa mtengo. Iye anadziŵa mmene ena a iwo amene anali kuyang'ana anachiritsidwira.

Kodi chinachitika ndi chiyani kwa amene sanali kuyang'ana pa njokayo ndi kukhala osachiritsidwa?

______________________________

==========================================================

12. Onse amene sanayang'ane pa njokayo ankafa. Anthu aku Israeli anachimwa. Njoka zinali kuŵaluma ndipo anali kufa. Ngati iwo anali kuya-

ng'ana pa njoka yapa mtengo anali kukhala ndi moyo. Koma ena sanali kuyang'ana pa njokayo. Mwina iwo sanali kukhulupirira kuti akhoza .kuthandizidwa pongoyang'ana pa njokayo. Iwo anali kungodwala kufikira kufa.

Ife tonse tinachimwa. Chilango cha tchimo ndi imfa. Yesu Khristu anakwezedwa pa mtanda. Iye anafera machimo athu. Ngati ife tiyang'ana kwa Yesu Khristu ndi kukhulupirira mwa Iye, timakhala ndi moyo. Kungoyang'ana kwa Yesu kokha sikukwanira. Ife tiyenera kukhulupirira mwa Iye.

Kodi ndi chiyani chidzaoneke kwa amene sakhulupirira mwa Yesu?

____________________________________________

===========================================================================

13. Iwo adzafa. Iwo adzafa m'matupi awo. Ndipo sadzakhala ndi moyo wauzimu. Iwo adzasiyanitsidwa ndi Mulungu kwa nthaŵi zonse. Iwo sadzalowa mu Ufumu wa Mulungu. Iwo sadzakhala ku nthaŵi zonse.

Kuchokera ku Mawu a Yesu kwa Nikodemo, kodi ndani amalandira kubadwa kwatsopano ndi moyo wosatha?

____________________________________

____________________________________________

===========================================================================

14. Aliyense amene akhulupirira mwa Yesu amalandira kubadwa kwatsopano ndi moyo wosatha. Limeneli ndi lonjezo lodabwitsa.

Kodi chidzaoneka ndi chiyani kwa amene sakhulupirira mwa Khristu?

____________________________________________________________

===========================================================================

15. Iwo adzafa. Chifukwa cha chimenechi ndi kofunika kuti ife timvetsetse chiphunzitso cha Yesu kwa Nikodemo. Ndi kofunika kwa ife kukhulupirira mwa Yesu Khristu. Yesu analalikiranso kuti anthu amayenera kulapa. Ife sitingathe kusunga machimo athu ndi kuyesa kukhulupirira mwa Yesu. Ngati titakhulupirira moona tidzatembenuka ku machimo athu.

Marko 1:14-15:

Yesu anadza ku Galileya, nalalikira Uthenga Wabwino wa Mulungu, nanena, "nthaŵi yakwanira, ndipo Ufumu wa Mulungu wayandikira; tembenukani mtima, khulupirirani Uthenga Wabwino:

Limeneli ndi phunziro lofunika koposa. Anthu anu afunika kudziŵa zinthu zimenezi. Konzani ulaliki oyenera kuulalikira kuchokera mphunziro la dzulo ndi lero. Papepala lina lembani zinthu zikuluzikulu zimene munganene. Lalikirani ulaliki umenewu ngati mungathe. Khalani okonzeka kudzauza kalasi za ulalikiwo.

==================================================================

16. Kuchokera m'mawu a Yesu kwa Nikodemo, kodi ndi ndani amalandira kubadwa kwatsopano ndi moyo wosatha? ____________________

____________________________________________________________

Kodi chidzaoneka n'chiyani kwa iwo amene sakhulupirira? ____________

==================================================================

1. Kwa masiku aŵiriŵa takhala tikuphunzira kubadwa kwatsopano.

Kuchokera m'mawu a Yesu kwa Nikodemo, kodi ndani amalandira kubadwa kwatsopano ndi moyo wosatha?

________________________________

Kodi chidzachitike ndi chiyani kwa iwo amene sakhulupirira? __________

===========================================================================

2. Aliyense amene akhulupirira mwa Khristu amalandira kubadwa kwatsopano ndi moyo wosatha. Amene sakhulupirira mwa Iye adzafa.

Atatha kulankhulana ndi Nikodemo, Yesu anapita ku Yerusalemu. Iye anali kupita m'dera la Yudeya ndipo anakhala kumeneko ali kuphunzitsa. Ndipo anachoka ku Yudeya namapita ku Galireya. Kumbukirani kuti Samariya ali pakati pa Yudeya ndi Galireya. Choncho Yesu anadzera mopyola ku Samariya. Tiyeni tiphunzire zinthu ziŵiri za mmene iye anachezera kumeneko.

(1) Ku Samariya Yesu poyamba analankhula kwa mkazi wochimwa pachitsime.

(2) Yesu anafuna kumupatsa Iye madzi amoyo, omwe ali moyo wosatha.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Yohane 4:3 mpaka 15. Kodi Yesu anapempha chiyani kwa mkazi waku Samariya?

____________________

===========================================================================

3. Iye anapempha madzi. Yesu ndi akuphunzira ake anafika mumzinda wa Sukali. Pafupi ndi mzindawo panali chitsime. Pamene mkazi anali kubwera kudzatunga madzi, Iye anamupempha madziwo kuti amwe.

Yohane 4:9:

Pamenepo mkazi wa m'Samariya ananena ndi Iye, "bwanji Inu muli Myuda, mupempha kwa ine kumwa, ndine mkazi Msamariya?

Kodi mkazi waku Samariyayo anadabwa kuti Yesu analankhula kwa iye?

______________________________________________

==================================================================

4. Inde. Iye anali wodabwa. Iye anadziŵa kuti Ayuda sanali kukonda a Samariya. Panalibe ubwenzi pakati pa Ayuda ndi a Samariya. Ayuda sanali kumwera zikho za Asamariya. Ndipo Msamariya ameneyu anali mkazi. Akazi anali wodedwa koposa amuna. Ayuda ambiri sanali kulankhulana ndi mkazi wa chi Samariya. Timaonanso kuti mkaziyo anali wochimwa kwambiri. Iye anali atakwatirana kale ndi amuna asanu. Ndipo iye anali kukhala ndi mwamuna amene sanali wake.

Kodi Yesu anakana kulankhula ndi mkazi waku Samariya kapena Iye analankhulana naye?

______________________________________________

==================================================================

5. Yesu analankhulana ndi mkazi ameneyu. Iye anali Msamariya. Iye sanali mkazi wabwino koma Yesu analankhula naye. Iye anamupempha kuti amuchitire kanthu kena. Iye anapempha madzi. Chimenechi ndi chinthu china chimene tiyenera kuchiganizira. Yesu sanadane ndi mkazi waku Samariya. Yesu sanali kudana ndi mtundu kapena pfuko lina lililonse ngakhale kuti iwo anali adani a Ayuda. Yesu sanadane ndi anthu ochimwa. Iye anabwera kudzapulumutsa onse pamodzi.

Kodi mkazi wa Msamariyayu anali wotani yemwe analankhula ndi Yesu poyamba?

______________________________________________

==================================================================

6. Iye anali wochimwa. Iye anali mkazi woipa. Yesu sanadane ndi aliyense. Ayuda anali ndi adani ambiri. Koma Yesu sanali kudana ndi pfuko kapena mtundu wa anthu. Iye sanadane ndi wochimwa. Iye anabwera kudzapulumutsa anthu ochimwa, amuna ndi akazi. Iye anabwera kudzapulumutsa pfuko ndi mtundu uliwonse wa anthu.

Kodi Yesu poyamba analankhula ndi yani m'Samariya? ____________________

==================================================================

7. Iye poyamba analankhula ndi mkazi wochimwa pa chitsime. Iye analankhulana naye. Iye anamupempha kuti amwe madzi. Popeza mkaziyo anali kutunga madzi analankhula naye za madzi. Iye anati akadakhoza kumupatsa kanthu kena.

Yohane 4:10:

> Yesu anayankha nati kwa iye, "Ukadadziŵa mtulo wa Mulungu ndi Iye amene ali kunena ndi iwe, undipatse Ine ndimwe; ukadampempha Iye, ndipo akadakupatsa madzi amoyo."

Kodi Yesu ananena kuti akadapatsa mkazi ameneyu chiyani?

____________________________________

==========================================================================

8. Iye anati adakampatsa madzi a moyo. Mkazi sanamvetsetse kuti chimenechi chinali kutanthauza chiyani. Iye anaganiza kuti Yesu anali kunena za madzi apachitsimecho. Yesu anamuthandiza kuti amvetsetse.

Yohane 4:13-14:

> Yesu anayankha nati kwa iye, yense wakumwako madzi aŵa adzamvanso ludzu; koma iye wakumwa madzi amene Ine ndidzampatsa sadzamva ludzu nthaŵi zonse; koma madzi amene Ine ndidzampatsa adzakhala mwa iye kasupe wa madzi otumphukira ku moyo wosatha."

Kuchokera ku Mawu a Yesu ameneŵa, kodi madzi a moyo akadatumphukira kukhala chiyani?

__________________________________________

==========================================================================

9. Akadakhala kumoyo wosatha. Moyo wosatha umatanthauza zinthu zambiri. Chimatanthauza kuti machimo athu akhululukidwa. Chimatanthauza kukhala aufulu kuchokera ku chilango cha uchimo. Chimatanthauza kukhala ndi mtendere ndi Mulungu ndi pakukhala ndi moyo wokondweretsa Iye. Kumatanthauza kukhala ndi Iye nthaŵi zonse.

Mkaziyo anaganiza kuti Yesu anali kulankhula za madzi adziko lapansi. Koma Yesu anali kulankhula za madzi a uzimu. Iye anati madzi ameneŵa akhoza kukhala moyo wosatha. Madzi a dziko lapansi sangapereke moyo wosatha. Koma madzi auzimu okha ndiye angachite zimenezi.

Kodi ndani amafuna kupereka madzi amoyo omwe ali moyo wosatha? ________

==========================================================================

10. Yesu amafuna kupereka madzi ameneŵa. Madzi ameneŵa siochokera ku chitsime ayi koma ochokera kwa Mzimu Woyera. Madzi ameneŵa ndi moyo wosatha komanso chikhululukiro cha tchimo. Ndi kukhala opulumutsidwa kuchokera ku chilango chosatha. Ndi moyo wosatha wochokera kwa Mzimu Woyera.

Kodi Yesu anatcha chiyani madzi a mtundu umene amafuna kupereka?

11. Iye amaŵatcha madzi amoyo. Chinthu chimene chili ndi moyo chimapitirirabe kukhala ndi moyo. Chimakula. Chimaonjezera kukhala bwino. Yesu anati tiyenera kumwa madzi ameneŵa. Ife tiyenera kulandira moyo wosatha umene Iye amafuna kutipatsa. Timaulandira pokhulupirira mwa Yesu Khristu. Ife timamwa pokhulupirira kuti Iye akhoza kutikhululukira machimo athu.

Nthaŵi zina kumakhala kovuta kupeza mawu ofotokozera zinthu za uzimu. Khristu amafuna kutipanga ife kukhala anthu atsopano. Iye amafuna kusintha miyoyo yathu. Mawu ambiri amagwiritsidwa ntchito kufotokozera zomwe Iye amatipatsa ife. Zina za izo ndi izi: Kubadwa mwatsopano, moyo wa uzimu, moyo wa muyaya, madzi amoyo.

Kodi Yesu amafuna kupereka madzi amoyo kwa yani omwe uli moyo wosatha?

12. Iye anafuna kupatsa mkazi wochimwa pachitsime. Mkazi ameneyu anafunika kuti akhale wopulumutsidwa kuchokera ku matchimo ake. Iye anayenera kukhulupirira mwa Khristu. Iye anayenera kulandira zomwe Yesu akadapereka.

Kodi Yesu adautcha chiyani moyo wosatha umene anafuna kumpatsa iye?

13. Iye amaŵatcha kuti ndi madzi amoyo. Yesu analankhulanso za madzi amoyo pa nthaŵi inanso. Nthaŵi zinanso anapita ku Yerusalemu kuti aka-

chite nawo phwando la paskha.

Yohane 7:37-39:

Koma tsiku lomaliza, lalikululo la phwando, Yesu anaimirira napfuula, ndi kunena, "ngati pali munthu akumva ludzu, adze kwa Ine, namwe. Iye wokhulupirira Ine, monga chilembo chinati, Mitsinje ya madzi amoyo idzayenda kutuluka mkati mwake." Koma ichi anati za Mzimu amene iwo akukhulupirira Iye anati adzalandire.

Kuchokera m'ndime zimenezi, kodi ndani amakhala mkati mwa okhulupirira monga madzi a moyo?

______________________________

==========================================================

14. Ndi **Mzimu** Woyera. Munthu amene amamulandira Iye sakhala ndi ludzu la moyo wa uzimu chifukwa ali ndi madzi amoyo. Iye amakhala ndi Mzimu Woyera amene amampatsa mphamvu ndi madalitso. Iye ali ndi moyo wosatha.

Kodi Yesu amautcha chiyani moyo wosatha umene anafuna kuupereka?

______________________________

==========================================================

15. Yesu anati akadakhoza kupereka madzi amoyo. Masiku anonso Iye ali kulonjeza zimenezi. Iye amati tiyenera kumupempha madzi amoyo. Tiyenera kumulandira Iye. Poyamba mkazi waku Samariya sanakhulupirire mwa Yesu. Koma Yesu anapitirizabe kulankhula naye. Iye anaphunzira zambiri za Iye.

Yohane 2:28-29,39:

**Pamenepo mkazi anasiya mtsuko wake,** namuka kumudzi, nanena ndi anthu, "Tiyeni mukaone munthu, amene anandiuza zinthu zilizonse ndinazichita: ameneyu sali Khristu nanga? ...Ndipo m'mudzi muja anthu anakhulupirira Iye chifukwa cha Mawu a mkazi, wochita umboniyo.

Kodi muli kuganiza kuti mkazi waku Samariya analandira madzi amoyo ndi moyo wosatha?

______________________________

==========================================================

16. Ife tikuganiza kuti iye analandira. Mwina inunso mukhoza kugwiritsa ntchito njira yomweyo pofotokozera abwenzi anu za moyo wosatha.

Kodi Yesu poyamba analankhula ndi yani m'Samariya? ______________

Kodi Yesu anautcha chiyani moyo wosatha umene Iye anafuna kuupereka?

______________________________________________

==========================================================

SABATA LACHINAYI: KHRISTU AYAMBA NTCHITO YAKE
TSIKU LACHISANU: IYE ANAKANIDWA KU NAZARETE

1. Taona kuti atangotha kukacheza ku Yerusalemu, Yesu anabwerera ku Galireya. Iye anadzera njira yomwe imadutsa m'Samariya.

Kodi Yesu analankhula kwa yani poyamba m'Samariya? ________________

Kodi Yesu anautcha chiyani moyo wosatha umene Iye anafuna kuupereka?

________________________________________

==================================================================

2. M'Samariya, Yesu poyamba analankhula kwa mkazi wochimwa pachitsime. Iye anamuuza kuti akhoza kumpatsa madzi amoyo. Mkaziyo anaitana anthu ena kuti abwere ndi kudzamvera kwa Yesu. Yesu anakhala masiku aŵiri akulankhula m'Samariya. Iye anali kuphunzitsa anthu. Ndipo Asamariya ambiri anakhulupirira mwa Iye.

Kenaka Yesu anapita ku Galireya. Ku Galireya Iye anapita mumzinda umene anakulira. Mzinda umenewu unali Nazarete. Tiphunzira zinthu ziŵiri zimene zinaoneka mu mzinda umenewu.

(1) Pamene Yesu analalikira m'Nazarete, anthu anamukana.
(2) Chitsanzo cha Yesu cha ku Nazarete chimatiphunzitsa kuti tizipitirizabe kuchita chifuniro cha Mulungu ngakhale anthu ali kudana nafe.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga zomwe zinachitika ku Nazarete. Werengani Luka 4:16 mpaka 30. Kodi anthu aku Nazarete anakhulupirira mwa Yesu?

________________________________

==================================================================

3. Iwo sanakhulupirire. Iwo anakwiya kwambiri ndipo anafuna kupha Yesu. Iwo anafuna kuti akamponye paphiri lalitali. Iwo sanafune kukhulupirira zinthu zimene Iye anazinena. Iwo sanamulandire Iye, ngakhale kuti umenewu unali mzinda umene Iye anakuliramo.

Kodi umenewu unali mzinda uti umene anthu anakana Yesu? ____________

==================================================================

4. Umenewu unali mzinda wa Nazarete. Unali mzinda umene Yesu anakuliramo. Anthu anali kumudziŵa Yesu, komabe anafuna kumupha. Iwo sanakhulupirire zimene Iye anali kunena. Iwo anamukana Iye. Koma ndi chifukwa chiyani iwo anachita zimenezi? Buku Lopatulika limatiuza izi.

Luka 4:16-21:

> Ndipo anadza ku Nazarete, kumene analeredwa; ndipo tsiku la sabata analoŵa m'sunagoge (kapena m'tchalitchi) monga anazoloŵera, naimiriramo kuŵerenga m'kalata ...ndipo anayamba kunena kwa iwo, kuti "Lero lembo ili lakwanitsidwa m'makutu anu."

Kodi Yesu anachita chiyani m'sunagoge? ____________

______________________________________________________________

==================================================================

5. Yesu anaŵerenga ndi kulankhula kwa anthu. Iye anakumana nawo pa tsiku la sabata. Yesu anali wokhulupirika pomapita ku tchalitchi. Anthu anamupempha kuti awerenge. Iye anaŵerenga mawu a m'neneri Yesaya.

Luka 4:17-18:

> Ndipo mmene Iye anafunyulula bukulo, anapeza pomwe panalembedwa, "Mzimu wa Ambuye uli pa Ine, chifukwa chake Iye anandidzoza Ine ndiuze anthu osauka Uthenga Wabwino: Ananditurna Ine kulalikira a m'singa mamasulidwe.

Yesu ananena kuti chinenero chimenechi chinali kukwaniritsidwa pamaso pawo. Kodi muli kuganiza kuti Yesu anali kutanthauza chiyani?

______________________________________________________________

==================================================================

6. Tidzakambirana tonse pamodzi. Ife tikhoza kunena kuti iye anaŵafunsa iwo kuti akhulupirire kuti Iye anali wokwaniritsa chinenero kapena ulosi. Ayuda anakhulupirira kuti mawu a Yesaya ameneŵa analankhula za

Mesiya. Iwo anakhulupirira kuti mfumu imene ikudzayo idzathandiza aliyense. Yesu anali kukwaniritsa chinenero chimenechi. Chinenero chinati, "Mzimu wa Ambuye uli pa Ine." Mzimu Woyera unadza nutera pa Ambuye pamene anali kubatizidwa.

Luka 4:14:

Ndipo Yesu anabwera ndi mphamvu ya Mzimu ku Galireya; ndipo mbiri yake ya Iye inabuka ku dziko lonse loyandikira.

Yesu anali kukwaniritsa chinenero cha Yesaya. Kodi anthu aku Nazarete anakhulupirira mwa Iye kapena anamukana Iye? ______________

==========================================================================

7. Iwo anamukana Iye. Iwo anamva zomwe anthu anali kunena zinthu zabwino za Yesu. Poyamba anthu aku Nazarete anali kunenanso zinthu zabwino. Koma nthaŵi iyi anakumbukira mmene Iye anali mwana mu mzinda wao.

Luka 4:22:

Nanena, "kodi uyu si mwana wa Yosefe?"

Iwo anali kuganizira kuti: Ife timamudziŵa munthu ameneyu. Wakulira mu mzinda mwathu muno. Timadziŵa bwino atate ake, Yosefe. Nanga Iye akhoza kunena bwanji kuti ali kukwaniritsa chinenero cha Yesaya? Iye akhoza kunena bwanji kuti iye ndi Mesiya?

Koma ife tikudziwa kuti Yesu akadakhoza kukwaniritsa chinenero. Kodi atate woonadi a Yesu ndi ndani? ______________

==========================================================================

8. Atate wa Yesu ndi Mulungu. Anthu aku Nazarete anaganiza kuti Yesu ndi mwana wa Yosefe. Koma Iye sanali wotero. Yesu ndi mwana wa Mulungu. Mulungu ndiye anadziŵa Atate ake okha. Yesu anadziŵa kuti anthu amu mzinda wake sangamukhulupirire. Iwo sangakhulupirire zozizwitsa zomwe Iye anachita mmalo ena.

Luka 4:23-24:

Ndipo anati kwa iwo, kwenikweni mudzati kwa Ine nkhani iyi, "sing'anga iwe tadzichiritsa wekha: zonse zija tazimva zinachitidwa ku Kapernao, muzichitenso zomwezo kwanu kuno." Ndipo Iye anati, "Indetu ndinena kwa inu, kuti, palibe mneneri

alandirika ku dziko lakwawo."

Pamene Yesu analalikira ku Nazarete, kodi anthu anachita chiyani?

______________________________________________

===================================================================

9. Iwo anamukana ndiponso anakana kukhulupirira mwa Iye. Iwo anafuna kumupha. Yesu anadziŵa mitima yawo. Iye anadziŵa kuti mneneri sangathe kulandiridwa ku dziko lake lomwe. Iye anadziŵa kuti anthu a m'dziko lake sadzamulandira. Iye ananena kuti mneneri Eliya ndi Elisa sanalandiridwe ndi anthu awo. M'njira yomweyo, Iye sakadalandiridwa ndi anthu aku Nazarete.

Kodi muli kuganiza kuti nthaŵi zonse masiku ano alaliki azilandiridwa ndi anthu am'mudzi mwawo?

______________________________

===================================================================

10. Nthaŵi zina iwo salandiridwa. Yesu anakanidwa ndi anthu akwawo. Izinso nthaŵi zina zimachitika kwa otsatira ake masiku ano. Iwo amakanidwa ndi anthu akwawo. Mwina iwo akhoza kuŵada ndi kuwapitikitsa. Izi ndi zimene zinaoneka kwa Yesu. Koma kodi zimenezi zinalepheretsa Yesu kuchita chifuniro cha Mulungu? Ayi, Iye anapita ku midzi ina ndi m'mizinda. Iye analalikira ndi kuchiritsa anthu. Anthu ambiri anamutsata Iye. Iye anachita chifuniro cha Mulungu ngakhale kuti anthu akwawo anamukana.

Ngati ife tikutsata chitsanzo cha Yesu, kodi tidzapitiriza kuchitabe chiyani ngakhale anthu akwathu akutikana?

______________________________

===================================================================

11. Tidzakhala tikupitiriza kuchitabe chifuniro cha Mulungu. Nthaŵi zonse anthu salandira Uthenga wa Mulungu. Ngati muli wa ntchito ya Chikhristu, abanja lanu lomwe akhoza kukukanani. Anthu aku mudzi wanu akhoza kukukanani. Koma izi siziyenera kukuletsani kuti muchite chifuniro cha Mulungu. Tiyenera kupitirizabe kuchita chifuniro cha Mulungu.

Tiyenera kupitirizabe kuchita chifuniro cha Mulungu ngakhale anthu akwathu atikane.

Pamene Yesu analalikira ku Nazarete, kodi anthu anachita chiyani?

______________________________________________

---

12. Pamene Yesu analalikira ku Nazarete, anthu anamukana. Iwo anakalipa chifukwa cha Iye. Iwo anafuna kumukankhira kumbali kwa phiri.

Luka 4:30-31:

> Koma Iye anapyola pakati pawo, nachokapo ndipo Iye anatsika nadza ku Kapernawo, ndiwo mudzi waku Galireya. Ndipo anali kuwaphunzitsa iwo pa sabata.

Kodi Yesu anapitiriza kuchitabe chifuniro chayani, pamene anthu aku Nazarete anamukana Iye?

______________________________________________

---

13. Iye sanalekeyi anapitiriza kuchita chifuniro cha Mulungu. Iye anapita ku midzi ina ndi kumizinda ina. M'madera ameneŵa Iye analalikira ndi kuchiritsa.

Kodi chitsanzo cha Yesu ku Nazarete chitiphunzitsa kuchita chiyani pamene anthu athu ali kutikana ife?

______________________________________________

---

14. Chimatiphunzitsa ife kuti tizipitiriza kuchita chifuniro cha Mulungu. Ife tikhoza kuchita monga momwe Yesu anachitira. Tikhoza kupita ku midzi ina kukalalikira. Ife tikhoza kutumikira Mulungu m'madera ena. Anthu akwathu akhoza kutikana. Koma chimenechi sichitanthauza kuti Mulungu watikananso ayi.

Pamene Yesu analalikira ku Nazarete, kodi anthu anachita chiyani?

________________________________________________________

============================================================

15. Iwo anamukana. Anthu aku Nazarete sanathe kukhulupirira mwa Yesu. Anthu a m'mudzi mwake sanamufune.

Kodi chitsanzo cha Yesu ku Nazerete chikutiphunzitsa chiyani ngati anthu akutikana?

________________________________________________________

============================================================

16. Tiyenera kupitiriza kuchita chifuniro cha Mulungu. Yesu anakanidwa ndi anthu akwawo omwe. Mwina zimenezi zimakuonekeraninso.

Idi ndi mlaliki wa mng'ono. Iye wakhala ali kuyesetsa kuthandiza anthu akwawo. Iye wakhala ali kulalikira m'mudzi mwawo. Iye wakhala ali kukonda anthu ndi kuwapempherera. Wakhala ali kuyesa kuŵauza za m'mene angabadwirenso mwatsopano. Koma iwo sanali kumvera. Nthaŵi zina iwo anali kufuna kumenyana naye Idi.

Lembani kanthu kena komwe muli kuganiza kuti Idi adayenera kuchita.

________________________________________________________

________________________________________________________

============================================================

17. Tidzakambirana za zimenezi tonse limodzi. Mwina Idi sanayese kupitiriza kwa nthaŵi yaitali. Iye mwina anayenera kukhala kwa nthaŵi yaitalipo. Kapena Idi anayenera kupita kumudzi wina. Kumeneko anthu mwina akadakakhoza kulandira uthengawo mwa chikondwerero.

Pamene Yesu analalikira mu Nazerete, kodi anthu anachita chiyani?

________________________________________________________

Kodi chitsanzo cha Yesu cha ku Nazarete chimatiphunzitsa kuchita chiyani ngati anthu athu akutikana?

________________________________________

________________________________________

SABATA LACHISANU: KHRISTU ATHANDIZA ANTHU
TSIKU LOYAMBA: YESU KHRISTU ALI NDI MPHAMVU YOPOSA ZIŴANDA

1. Sabata yapita tinaona mmene Yesu anayambira ntchito yake. Sabata ino tikhala tikuona mmene Iye anapitirizira ntchito yake. Tiona mmene Iye anathandizira ndi kuphunzitsa anthu.

Pamene Yesu anaphunzitsa ku Nazarete, kodi anthu anachita chiyani?

______________________________________________

Kodi chitsanzo cha Yesu chaku Nazarete chimatiphunzitsa kuchita chiyani ngati anthu ali kutikana? ______________________________

______________________________

==============================================================================

2. Pamene Yesu analalikira ku Nazarete, anthu anamukana. Koma Yesu sanasiye kulalikira. Zimenezi zimatiphunzitsa ife kuti tizichita chifuniro cha Mulungu ngakhale pamene anthu ali kutikana.

Kuchokera ku Nazarete, Yesu anapita ku Kapernao. Umenewu unali mzinda wina wa ku Galileya. Apanso Yesu anapita ku sunagoge kapena kuti ku tchalitchi. Kumeneko anachotsa chiŵanda mwa munthu. Zimenezi zinali zodabwitsa. Zimatiphunzitsa ife zinthu ziŵiri.

(1) Timadziŵa kuti Yesu ali ndi mphamvu kuposa ziŵanda chifukwa Iye anazitulutsa mwa anthu.

(2) Kudziŵa za zimenezi kumatithandiza kukhulupirira Khristu kuti Iye akhoza kutimasula kuti tisaope ziŵanda.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Luka 4:31 mpaka 41. Werenganinso ndime 33. Kodi ndi chiyani chinavuta mwa munthu amene anapfuulayo? ______________________________

==============================================================================

3. Munthu ameneyu anali kuvutika chifukwa cha ziŵanda. Ziŵanda zinamutsogolera iye kuchita zinthu zimene sanali kufuna kuchita. Zidamupanga kuti iye aope Yesu. Taonani zimene ziŵanda zinanena kupyolera mwa munthu wina.

Luka 4:34:

"Ha tiri ndi chiyani ndi Inu, Yesu wa ku Nazarete? Kodi munadza kutiononga ife? Ndikudziwani Inu muli yani, ndinu Woyera wake wa Mulungu?

Kodi ziŵanda zinadziŵa kuti Yesu ndani? ______________________________

==========================================================================

4. Ziŵanda zinamudziŵa Yesu. Izo zidamuitana dzina lake. Zinanena kuti Yesu ndi Woyera wa Mulungu. Zinali kuchita mantha ndi Yesu. Zinazindikira kuti Yesu ali ndi mphamvu yoziposa izo.

Luka 4:35:

Ndipo Yesu anam'dzudzula iye, nanena, "Tonthola, nutuluke mwa iye." Ndipo chiwandacho mmene chinamgwetsa iye pakati, chinatuluka mwa iye chosam'pweteka konse.

Pamene Yesu anauza chiwanda kuti chituluke, kodi chiŵanda chinachita chiyani?

______________________________________________________________

==========================================================================

5. Chiŵanda chinatuluka. Chinamvera Yesu. Chinadziŵa kuti chiyenera kuchita zomwe Yesu ananena. Yesu sanalore kuti ziŵanda zizipitiriza kuchita ntchito zawo zomwe zinali kufuna. Iye sanazilole kuti zilape. Iye sanazikhululukire. Nthaŵi zonse anali kuzitulutsa.

Kodi Yesu ali ndi mphamvu yoposa ziŵanda? ____________________________

==========================================================================

6. Inde, Iye ali ndi mphamvu yoposa ziŵanda. Iye ali ndi mphamvu yoposa zinthu zonse. Kumbukirani kuti Yesu anali m'sunagoge ku Kapernao. Anthu anaona kuti Iye anali ndi mphamvu. Iye anakhoza kuziuza zomwe anayenera kuchita. Iye anayenera kulandira ulemu. Ngakhale ziŵanda zinamumvera Iye.

Luka 4:31-32:

Ndipo anali kuwaphunzitsa iwo pa sabata, ndipo anadabwa ndi chiphunzitso chake, chifukwa mawu ake anali ndi ulamuliro.